BUKU ILI LIKASOWA, CHONDE BWEZANI KWA:

_____ ***FONI:*** _____

STRATEGIC IMPACT
SUKULU YOCHULUTSA AZITSOGOLELI ©

Q1

Phunzilo 1-10
v1.1.2 (2011)

STRATEGIC IMPACT
P.O. BOX 830337
RICHARDSON, TX 75083
WWW.TOUCHINGEVERYNATION.COM

© Permission to copy with attribution

NDONDOMEKO

Mau oyamba *4*
Mau mwachidule pa utumiki wa Strategic Impact *6*
Sukulu Yochulutsa ukatswili wa Atsogoleli *7*
Mfundu khumi zoyambila kuchulutsa Ophunzila opereka uthenga Mziko lanu *8*
Zofunikila za M' gulu iliyonse ya Sukulu Yochulutsa Atsogoleli *11*
M'ndandanda wa Kawerengedwe kamalemba *12*
Regesitala ya Gulu *14*
Mafunso aungwilo yapagulu *15*
Phunzilo 1 - Utukula za Umunthu wathu *"Maziko Amau Amulungu"* *16*
Phunzilo 2 - Ukukula Utsogoleli: *"Kudi utsogoleli utanthauza chiani?"* *18*
Phunzilo 3 - Ubyala mipingo: *"Mfundo 1:Sinthani maganizo anu"* *20*
Phunzilo 4 - Utukula za Umunthu wathu: *"Dzadzani`umoyo `wanu ndi mau Amulungu"* *24*
Phunzilo 5 - Ukuza Utsogoleli: *"Kudi Mstogoleli ndi ndani?"* *28*
Phunzilo 6 - Ubyala mipingo: *"Mfundu 2:Pemphelo* *30*
Phunzilo 7 - Utukula za Umunthu wathu: *"Mowelengela mau Amulungu"* *34*
Phunzilo 8 - Utukula za Utsogoleli: *"Chikhalidwe: The Essential Quality of a Leader"* *38*
Phunzilo 9 - Ubyala mipingo: *"Mfundu 3 & 4: Sonkhanisani ndiku phunzitsa gulu"* *40*
Phunzilo 10 - Utukula za Umunthu wathu: *"Pemphero ya chitsanzo"* *44*
Zolemba *48*
Version Release Notes *52*

Mau Oyamba

Masomphenya a Strategic Impact ndiku mphunzitsa atsogoleli omwe amene azamphudzitsa azitsogoleli ena ache kuti achulutse UPHUNZILA amene azachulutsa mipingo. Pamene mipingo zichulukila ndi Ophunzila, uthenga wa Mulungu udza alikidwa kwa anthu onse apadziko lapanse ndipo chikhalidwe cha Ufumu wa Ambuye Yesu chizakhazikitsidwa padziko lonse lapansi.

Nchito yomphunzitsa uchulutsa azitsogoleli ndi Ophunzila siuchitika pachabe kapena mwama chitachita. Kukhala mtsogoleli wa umulungu ndiponso ochulukila sikutha ai. Tifunikila kuwelenga mau Amulungu, upemphela, ndiku gonjela Ambuye Yesu. Tifunikilanso unkhala anthu oziletsa ndiponso odalila Mzimu Oyela. Izizi zimachitika pakati pa gulu la Akristu anzathu – omwe amene tiyanjana nao ndiku limbisana nao.

Mchipangano Chatsopano, buku la Machitidwe itisonyeza momwe Ufumu wa Mulungu unachulukila kwakukulu pachiyambi paja. Itisonyeza nchito za Mzimu Oyela kupyolela mwa Akristu, pamene iwowa ananvelela Mulungu ndikupeleka ulaliki ku Yelusalemu, Yudeya, Samalia kufikila kumalekedzelo adziko lonse lapansi.(1:8). Pamene Akristu adapeleka uthenga wa Mulungu kwa anthu apadziko, tiona chiyambi chachimango cha mpingo. Choyamba, tiona mpingo waku Yelusalemu, Machitidwe1-7 ionanso mpingo waku Antioke (Machitidwe 11-13) ndiponso mipingo inanso imene MtumwePaulo anabyala (Machitidwe14-20).

Modzi wa Mipingo yochititsa chidwi ndi Mpingo waku Aefeso. Pamene Paulo anali ku Efeso, Machitidwe19:9-10 itisonyeza kuti Paulo “anatenga Ophunzila ndiku wa phunzitsa mau Amulungu tsiku ndi tsiku m’sukulu yo chedwa Turano. Paulo anachita chomwecho pazaka ziwili kotelo kuti Ayuda ndi Ahelene akukhala m’Asiya anamva mau a Ambuye.” Kupyolela sikulu ya Turano”Paulo anachulutsa Ophunzila ndipo wowa anapita ndiku byala Miphingo Mmalo ya Chi Roma ya Asiya kotelo kuti anthu onse a mdela lonse analandila uthenga wabwinol! Chokondweletsa kwambili!

Mmodzi wa Ophunzila ochulukila ndi Epafra. Chikuoneka ngati kuti Epafra atakhala M’kristo, anaphunzitsidwa ndi Paulo ku Efeso panthawi imeneyi. Epafra anapita kumuzinda wa Kolose, Mzinda wa Mmalo a Asiya (Chikuoneka ngati uku ndiku kumudzi kwake) ndiku lalikila Uthenga Wabwino kudela lonse ndikuyambanso mipingo yatsopano kumalo yapafupi ya m’Herapoli ndi m’Laodikaya (welengani Akolose 1:6-7; 2:1; 4:12-13). Tidziwa kuti kulingana ndi Ndime izi, tiona kuti Paulo sanafikile malo awa ai (2:1), komabe tipeza kuti Mipingo idabyalidwa chifukwa cha ulaliki wamene unapelekedwa ndi Paulo ku Efeso.

Malemba yatsonyedzanso kuti ena mwa io amene analandila uthenga ndikupunzitsidwa ndi Paulo, anatumidwa ku Aroma ukathandiza uyamba m’pingo yatsopano (welengani Aroma 16:5 imene ichhula Epenetus, amene anali oyamba kulandila uthenga ku mzinda wa Asiya pambuyu pa ulaliki wa Paulo.

Nchito ya Ulaliki imene idapasidwa kwa ise ndi Ambuye Yesu pamodzi ndi chitsanzo cha ”Sukulu ya Turano” ku mzinda wa Efeso, ndicho chitsanzo cha “Sukulu yathu Yochulutsa Atsogoleli” Sukulu iyi ili m’manja yanu. Ngati muli ndi buku ili, chitanthauza kuti inu munatengako kale mbali ku maphunzilo ya THRUST. Pemphero yathu ndiyakuti Mulungu atukula ndikulimbitsa Umoyo wanu ndipo kuti mwaphunzilanso zina zache zazikulu. Tikhulupirira kuti mudamva ndiponso mudaphunzila pa za “Mfundo chumi zoyambila kuchulutsa Ophunzila opereka Uthenga mziko lanu.” Tikhulupiriranso kuti Mulungu adasewenza ndi inu pamodzi ndi Abale ena pomwe munapereka ulaliki kwa anthu otayika ndiku byala mipingo m’dela lanu.

Ukula ndi kutukuka kwanu mwa nchito iyi sikunathe ai! Mufunikila kupitiliza nozipereka muzi nchito zimenezi. Upezeka kum’sokhano wa “THRUST” chinali chabe chiyambi. Nichofunikila kuti mupitilize upita patsogolo ngati Atsogoleli. Maphunzilo awa Asanu ndi Atatu ya ikidwa kuti ya limbitse zomwe munaphunzira pa nthawi wa THRUST. Maphunzilo aya ya ima pa mfundu zitatuzi:

1. Utukula za Umoyo wathu
2. Utukula utsogoleli
3. Ubyala mipingo

Phunzilo iliyonse ida ikidwa kuti ithe pa sabata imodzi chabe. Maphunzilo yonse chumi yadaikidwa kuti yathe paminyezi Itatu chabe. Muzafunikila kuti mukumane kamodzi sabata iliyonse pamodzi ndi Abale Am’gulu lanu kuti muchite zamaphunzilo anu ndikuyankha mafunso yomwe yazafunsidwa. Pambuyo pache ndichofunika kuti nuyo pa inu nokha mutsilize zotsalila ndi zina zache zofunukila zam’gulu lanu. Samalani kuti mwakwanilitsa zonse zofunikila. Chimenechi chikhalidwe chizathandiza kuti timvetse cho onadi ndiponso ku chichita.

Potsiliza, osalola kuti zimene inu mukuphunzila kuti zithele kwa inu nokha ai. Pomwe nu mutatsiliza maphunzilo ya minyezi itatu yoyamba, tasamalani kuti mwa sankha Awiri Kapena anthu okwanila Asanu chabe omwe muzaphunzitsa. Chonde sewenzetsani buku ili kuti muphunzitse ndiku chulutsa Ophunzila. (Tizalankulanso zambiri pomwe tipitiliza ndi maphunzila athuwa).

Mulungu akudalitseni pamene mukupeleka uthenga kwa anthu onse apadziko lapansi.

Gulu la Atsogoleli a Strategic Impact

STRATEGIC IMPACT

"Umphunzitsa amitundu kuti abalalitsi uthenga padziko lonse"

UTUMIKI WATHU:

Tku mpunzitsa azitsogoleli amene achulutsa ophunzila amene azayamba nchito yo byala mipingo kwa anthu onse amitundu kuti tikwanilitse ulaliki kwa amitundun.

"AlMphamvu zonse zapatsidwa kwa ine kumwamba ndi pa dziko lapansi . Chifukwa cace mukani, phunzitsani anthu amitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate , ndi la Mwana ndi la Mzimu Oyera. Ndi kuwaphunzitsa ,asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulilani inu ; ndipo onani , ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano." Mateo 28:18-20

MAPULANO:

To multiply church planting disciples in every major city of the 12 major regions of the world.

"(Paulo)anawachokera, napatusa akuphunzira nafotokozera masiku onse m'sukulu ya Turano. Ndipo anachita comwecho zaka ziwiri; kotero kuti nonse akukhala m'."
Machitidwe 19:9-10

NJILA:

. **SEMINALA YOPEREKA MASO MPENYA (VS)** - Msonkhano watsiku limodzi chabe ya Azibusa ndi Azitsogoleli ena amumi pingo ya mudela lanu. Msonkhanu uyo ndi odziwitsa anthu pa za nchito ya Strategic Impact. Maphunzilo wathu ya yangana pa ziphunzitso izi:

1. Utukula za Umunthu wathu
2. Utukula Utsogoleli
3. Njila zo byalila Miping

I. **LMSOKHANO WA AZITSOGOLELI (LT)** - uyu ndi msokhano wochitika sabata lathunthu komwe tima phunzitsa azitsogolelir ~azibusa okwanila ngati 50 iamene ali ozipereka kuti apereke uthenga kwa osowa . maphunzilo aya ya yanganila mbali zitatu zazikulu ndi kumanga mipingo pamodzi.

II. **SUKULU YOCHULUTSA AZITSOGOLELI (SML)** - sukulu ya zaka ziwiri, chiphunzitso chili ndi maziko yache mu mau Amulungu, yoyanjanitsa abale ndi chiphunzitso chopitiliza maphunzilo munjila zitatu ndi ku bweletsa ungwilo kwa azitsogoleli ndiku chulutsa azitsogoleli.

- Chiyanjano - *Mtsogoleli aliyense atengako mbali mugulu 'Yositha Za umoyo' ndiku khuzana wina ndi mzache ndiku funsananso mafunso ya Ungwilo.*
- Uziphunzitsa - *"Ngati ungawerenge chinthu, ungachitsogolele." Komabe dela iliyonse ili ndi mtsogoleli woyang'anila kuti zinthu zikuyenda bwino*.
- Ulaliki - *Membala aliyense wa m'gulu afunika ulalika uthenga kamodzi pa sabata.*
- Kasewenzese - *Kulibe munthu azaloledwa upitiliza maphunzilo yapamwanba asana silize zamaphunzilo yoyamba.*
- Zopitiliza - *Maphunzilo aya yana ikidwa kuti yachitike sabata iliyonse pa zigao za minyezi makumi yawiri ndi yasanu ndi yawiri- 9 Quarters (2 years, 3 months),minyezi itatu iliyonse ili ndimaphunzilo khumi.*
- Uchulutsa - *Pamene otengako mbali apita ku chigawo chachibili chamaphunzilo yao, yense wa azitsogoleli afunikila ubweletsanso Azitsogolele ena awiri omwe amene azayamba chigawo choyamba chamaphunzilo. Mtsogoleli aliyense azafunikila uchita chodzimodzi asana pite ku chigawo chachiwiri chamaphunzilol.*
- Ukula - *Azitsogoleli onse amene agwila manso mphenya apita kumadela ena ndiku chitanso chimodzimodzi monga anamphunzila.*

V. **FAN-THE-FLAME CONFERENCE (FTFC)** - An annual Conference for staff, leaders, and multipliers for feedback, discussion, encouragement, equipping, and strategy held in each major region of the world.

Strategic Impact

School of Multiplying Leaders

Each Leader at the end of the first quarter invites 2 new leaders

10 Lessons per Quarter

Generations

First SML	1st	2nd	3rd	4th	5th	6th	7th	8th	9th	Each shares the Gospel 1x per week	Total Leaders Involved
Quarter 1	25									250	25
Quarter 2	25	50								750	75
Quarter 3	25	50	100							1750	175
Quarter 4	25	50	100	200						3750	375
Quarter 5	25	50	100	200	400					7750	775
Quarter 6	25	50	100	200	400	800				15750	1575
Quarter 7	25	50	100	200	400	800	1600			31750	3175
Quarter 8	25	50	100	200	400	800	1600	3200		63750	6375
Quarter 9	25	50	100	200	400	800	1600	3200	6400	127750	**12775**
										Total	**253250**

Generations

Second SML	10th	11th	12th	13th	14th	15th	16th	17th	18th	19th	20th	21st … etc.	Total Leaders Involved
Quarter 10		50	100	200	400	800	1600	3200	6400	12800			25550
Quarter 11				200	400	800	1600	3200	6400	12800	25600		51000
Quarter 12					400	800	1600	3200	6400	12800	25600	51200	102000
Quarter 13						800	1600	3200	6400	12800	25600	etc.	etc.
Quarter 14							1600	3200	6400	12800	25600	etc.	etc.
Quarter 15								3200	6400	12800	25600	etc.	etc.
Quarter 16									6400	12800	25600	etc.	etc.
Quarter 17										12800	25600	etc.	etc.
Quarter 18											25600	etc.	etc.

MFUNDO KHUMI ZOYAMBILA KUCHULUTSA OMPHUNZILA OPERAKA UTHENGA MZIKO LANU (v2.1)

MFUNDO 1: SINTHANI MAGANIZO ANU

Sinthani maganizo anu a‘ kumanga mpingo wanga‘ ndiganizo lofikila dela lanu, dziko lanu kapena dziko lonse lapansi ndi uthenga wa Mulungu
(Mateyo 28:18-20; Machitidwe 1:8; Machitidwe 20:24)

MFUNDO 2: PEMPHERO

PEMPHERERANI anchito okolola za m’munda!
(Luka 10:2; Machitidwe 13:1-3)

MFUNDO 3: ONETSANI MASO MPHENYA

Onetsani maso mphenya opereka uthenga wa Mulungu ku dela lanu. (Machitidwe 1:8; 13:1-3)

MFUNDO 4: SONKHANITSANI NDIKU MPHUNZITSA GULU

Zindikilani,sankhani, SONKENITSANI NDI KUMPHUNZITSA gulu la anthu ndi kuchulukitsa kawili caka chilichonse. (Machitidwe 14:21-28; 19:9-10; Akolose 1:7; 2 Timoteo 2:2)

MFUNDO 5: SANKHANI MALO

Mwapemphelo,Sankhani Malo Kapena Gulu La Anthu Omwe Mulungu Akukutsogolelani
(Machitidwe 16:6-40)

A. Zindikilani komwe Mzimu Oyela akukutsogolelani kuti muyambe mpingo watsopano kuti muwafikile ndi mau a Mulunngu.
B. Fufuzani zofunikila, ndizina zache zovuta zimene zingakhuze mpingo watsopano.

MFUNDO 6: LALIKILANI

Lalikilani uthenga kwa anthu am'malomo. (Machitidwe 5:42; 14:21,25; 20:20)

MFUNDO 7: MPHUZITSANI AKRISTU ATSOPANO

Mpunzitsani akristu atsopano mumagulu ya awili kapena atatu. (Machitidwe 14:22; 20:20)

MFUNDO 8: SONKHANITSANI AKRISTU ATSOPANO

Sonkanitsani akristu kuti:

A. Muwalandile ndiku yanjana nao,
B. Mulambile ndiku pemphela nao,
C. Mpunzilani mao pamodzi nao,
D. Ndikutumikila kapena kupeleka umboni pamodzi nao.

(Machitidwe 2:42,46; 12:12; 16:40; Aroma 16:15; 1 Akolinto 16:19, Akolose 4:15)

MFUNDO 9: CHULUTSANI OMPHUNZILA

Chulutsani Omphunzila ndi kuchitanso mfundo zimene taika. (1 Atesalonika 1:7-8)

MFUNDO 10: GWILIZANANI MANJA KUTI MUYAMBE UTUMIKI

Gwilizanani pamodzi, azibusa ndi azitsogoleli ena onse kuti muyambe utumiki olalikila uthenga wa Mulungu.

MTSOGOLELI WAGULU LATHU NDI:

Dzina: _____ Foni: _____

ANTHU AMGULU LANGA NDI AWA:

Dzina: _____

Foni: _____ email: _____

Dzina: _____

Foni: _____ email: _____

Dzina: _____

Foni: _____ email: _____

Dzina: _____

Foni: _____ email: _____

MISONKANO YATHU IZAKHALA MOTELE:

Malo okumanila: _____

Tsiku: _____ Nthawi: _____

TAMVANA KUWELENGA MALEMBA AWA:

Machapitala awa patsiku iliyonse: _____

Kuyambila (Malemba a Buku): _____

SCRIPTURE READING LOG:

TSIKU	NDIME

TSIKU	NDIME

GROUP MEETING ATTENDANCE RECORD:

TSIKU	Phunzilo	Participants Present

*GROUP ACCOUNTABILITY QUESTIONS**

MAFUNSO AYA YA IKIDWA KUTI YATHANDIZILE KHALIDWE NDI UMOYO OWULULILA MACHISMO. NDI CHOFUNIKILA KWAMBIRI KUTI TIFUNSE NDI KUYANKHA MOKHULUPILIKA NDIPO MWA CHISOMO NDICHISINSI ZONSE ZOLANKHULIDWA MUGULU LANU NDI ZACHISINSI NDI CHOSALOLEDWA KULANKULA NDI ENA ACHE.

1. **KODI UMBONI WANU SABATA LINO UNALI WA BWINO NDIPO OSONYEZA UKULU WA YESU KRISTU MUMAKAMBIDWE KAPENA MUMA CHITIDWE YANU?.MWALANKHULA NDI YANI UTHENGA WA AMBUYE YESU?**

2. **KODI MWA WELENGA KAPENA KU KUPENYELELA ZITHUNZI ZOSAYENELA MONGA ZA MALISECHE KAPENA ZINA ZACHE ZONYANSA MWINA MWACHE KUKHALA NDI MAGANIZO ACHIWELEWELE KAPENA YA DAMA SABATA LINO?**

3. **KODI MUNALEPHELA KU SONYEZA UNGWILO MUNJILA YA NDALAMA KAPENA KUKHUMBA ZAENA SABATA LINO?**

4. **KODI MWASONYEZA CHIKONDI KWA ANTHU MONGA M`BANJA, ABWENZI,ANANSI NDI AKRISU SABATA LINO?**

5. **KODI MWA ONONGA ANTHU ENA NDI MAU ANU MWAMJEDO KAPENA NDI MAU OWAWA SABATA LINO.**

6. **KODI MWAGONGELA KUKHALIDWE ILIYONSE YO NYASA MULUNGU UNO?**

7. **KODI MWA KALABE NDI MUKWIYO KAPENA KUSA KULULUKILA ENA SABAA LINO?**

8. **KODI MWASILIZHA KUWELENGAMALEMBA YA SABHATA LINO (NDICHOYENELA KUTI MUMVANE PAZA MALEMBA SABATA ILI KU BWELAYI?**

9. **KODI MWACHITA ZO FUNIKA SABATA LINO?**

10. **TATI FOTOKOZELANI ZAZAKULU ZIMENE MWAPUNZILA.**

11. **NDI VUTO YANJI YAMENE MWAPEZA PO CHITA ZI NCHITO ZO? CHIFUKWA NINJI ZINAVUTA.**

12. **KODI MWANDIYANKHA MO KULUPILIKA ZAMENE NAKUFUNSANI?**

ADAPTED FROM "LIFE TRANSFORMATION GROUPS", PUBLISHED BY CHURCH MULTIPLICATION ASSOCIATES

Pamene muyamba ukumana, gawanikani m'magulu ya anthu ANAI pagulu limodzi pampindi zokwanila ngati makumi yatatu mwina mwache mochepekela. Muphephererani wina ndi mzache ndipo mufunsane mafunso ya ungwilo. Pambuyo pache nkhalaninso m'magulu anu ndiku werenga phunzilo ili ndiku ponyapo ndemanga.

Mu za umoyo wathu , kulibe tsankho imene imakhuza za umoyo wathu upambana sankhu yo nkhala ndi kuyanjana ndi Mulunguuch tsiku ndi tsiku. Tiyenela uyanjana nae Mulungu kopyolela m'mau ache. Mfumu Davide anali munthu ofunitsitsa mulungu Anali ozipeleka mwathunthu kwa Mulungu. Masalimo119 itisonyeza zimenezi.

TAONANI CHIYAJANO CIMENE MFUMU DAVIDE ANALI NACHO NDI MAU A MULUNGU:

Nelengani mau otsatila ndipo muyanke mafunsowa mujila yanu:

> **"Ndinakufunani ndi mtima wanga wonse;**
> **Ndisasokere kusiyana nao malamulo anu." [Masalimo 119:10]**

> **"Mtima wanga wasweka ndi kukhumba,**
> **Maweruzo anu nyengo zonse." [Masalimo 119:20]**

> **"Ndikondadi cilamulo canu;**
> **Ndilingalilamo ine tsiku lonse." [Masalmo 119:97]**

NDEMANGA/MAFUNSO: *INNDI NJILA ZOTANI ZOMWE DAVIDE ANA SONYEZA NJALA TKU MAU AMULUNGU?*

Nelengani malemba awa pamodzi:

> **"Cilamulo canu cikadapanda kukhala cikondweretso canga;**
> **ndikatayika m'kuzunzika kwanga." [Masalmo 119:92]**

> **"Cilamulo ca pakamwa panu cindikomera**
> **koposa golidi ndi silva zikwizikwi" [Masalmo 119:72]**

> **"ndidzakwezanso manja anga ku malamulo anu,amene ndiwakonda;**
> **ndipo ndidzalingalira pa malemba anu." [Masalmo 119:48]**

NDEMANGA/MAFUNSO: *Kodi CHIKHALIDWE cha Davide ku mau aMulungu chinali chotani?*

Nelenganinso malemba awa pomodzi:

“akukonda cilamulo canu ali nao mtendere
wambiri ndipo alibe cokhumudwirtsa.” .[Masalmo119:165]

“ndinawabisa mau anu mumtima wanga,
kuti ndsalakwire inu” [Masalmo119:11]

“citonthozo canga m’” kzunzika kwanga ndi ici;
Pakuti mau anu anadipatsa moyo.” [Masalmo 119:50]

NDEMANGA/MAFUNSO: *Kodi ndizotani <u>ZAPHINDU</u> zimene Davide anapeza <u>MUMAU</u> Amulungu?*

Fotokozelani Abale Amgulu lanu phindu lalikulu limene inu mwapeza Mmau Amulungu

<u>ZOCHITA SABATA LINO:</u>

Tsiku 1: KODI MUKULONJEZA <u>kuwerenga mau aMulungu tsiku ndi tsiku?</u>
Talemban lonjezo lanu kwa Mulungu:

Tsiku 2: Mwachindunji, kodi **ndiliti** pomwe muzayamba ufufuza Mulungu mu mau ache tsiku ndi tsiku? Lembani izi mwam’ndandanda wanu tsiku ndi tsiku.

Tsiku 3: Kodi ndikuti komwe muzakonzela malo yowerengela mau aMulungu tsiku ndi tsiku? Sankhani malo panyumba panu, ku Ofesi kwanu kapena malo yena yaliyonse ponye muzayamba kuwerengela mau mwachizowelezi. Malo achizowelezi ndiyofunika kuti ichi chichitike.

Tsiku 4: Kodi muzasewenzesa njila yanji pakawerengedwe ka mau aMulungu

Pamene muyamba ukumana, gawanikani m'magulu ya anthu ANAI pagulu limodzi pampindi zokwanila ngati makumi yatatu mwina mwache mochepekela. Muphephererani wina ndi mzache ndipo mufunsane mafunso ya ungwilo. Pambuyo pache nkhalaninso m'magulu anu ndiku werenga phunzilo ili ndiku ponyapo ndemanga.

Azimai ndi azibambo ambiri ali ndi phaso ya utsogoleli komabe sapeza ndanga yosewenzetsa patso yau tsogoleli. Kuti ise tikwanilise chifuniro cha Mulungu pa umoyo wathu, tifunikila utukula nkhalidwe yau tsogoleli . patsiku ya lelo tiyeni imvetsetsetse chikhalidwe cha utsogoleli. Mfunso ya ikulu ndi iyi is:

KODI UTSOGOLELI NDI CHIANI?

Chimasukilo chapafupi ndi ichi: **Utsogoleli ndiku takasa anthu kuti achite zomwe zaikidwa.** Kuli zikhalidwe zitatu zofunilkila pa umoyo wa utsogoleli; choyamba Utsogoleli ndi kutakasa anthu. Chachiwiri, Utsogoleli ndiku takasa anthu. Chachitatu, Utsogoleli utanthauzanso lingo. Utsogoleli ndiku takasa anthu kuti achite zomwe za kidwa.

NDEMANGA/MAFUNSO: *Tati uzani za umoyo wa mtsogoleli amene amakulimbitsan kapena ukutakasani. Kudi anachita bwanji? Wkodi ndizotani zomwe iwo anachita kapena zomwe analankhula zimene zinaku takasani mu umoyo wanu?*

Ngati ulephela utakasa anthu kuti akutsatile ndiye kuti sindiwe mtsogoleli! Komabe utsogoleli sikutakasa anthu chabe. Kuli anthu ambiri omwe angachite zimenezi. Kulinso azitsogoleli amene anatakasa anthu kuti achite zoipa.

NDEMANGA/MAFUNSO: *Kodi mungathe uti uzako zitsanzo za azitsogoleli akali omwe anatakasa anthu kuti achite zoipa kapena? Kodi munga ti uze atsogoleli ena omwe anatakasa anthu uchita zabwino?*

Mtsogoleli ali yense wo opa Mulungu afunikila akhale ndimaso mphenya yochokela kwa Mulungu kuti akwanilitse chifunilo cha Mulungu padziko lapansi .Lingo ili machokela pambuyo pokhala ndi maso mphenya yamene Mulungu anapatsa. Mtsogoleli aliyense wo opan Mulungu ali ndi lingo imodzi- ulalikila uthenga kwa onse osowa. Komabe,ndichofunikila kudziwa kuti lingo ndi maso mphenya yathu yalingana ndi chifunilo cha Mulungu. Kuti ise tidziwe chimenechi tifunika uzipereka mwa pephelo kwa Mulungu, uperekanso nthawi ndi maganizo yathu.

NDEMANGA/MAFUNSO: *Ndi lingo yotani yomwe Mulungu aku itanani kuti muchite panthawi ino kapena pamalo yano? Kodi lingo imeneyi ivomelezana ndi lingo yolalika uthenga kwa osowa? Mateo28:18-20*

Motsiliza:

Ngati ulibe mchangu, ulibe UTSOGOLELI.
Ngati ulibe Anthu, ulibe UTSOGOLELI.
Ngati SIUKWANILISA zofunika PANCHITO, ulibe UTSOGOLELI.

ZOCHITA SABATA LINO:

Tsiku 1: talingalilani zinthu zimene azitsogoleli amachita kuti minu mutakasidwe ndiku tengako mbali. Talembani zinthu zambiri zimene zisonyeza chikhalidwe cha munthu odziwa utakasa ena:

Kudi mzatani inu kuti mukhale ndi chikhalidwe chodziwa utakasa ena?

Tsiku 2: Ndi anthu oti amene MULUNGU alikuku itanani kuti inu mupereke utsogoleli?

Nichifukwa ninji inu muli mtsogoleli wao?

Tapimani ngati anthu ali afunisisa utsogoleli wanu kapena yayi. Mungawa takase bwinji anthu kuti akutsatileni inu?

Tsiku 3 and 4: Tengani masiku awiri yakuti mupephere ndiku fufuza nkope ya Mulungu kuti akupatseni zimene mufunikila kuchita panthawi inu ndi pamalo yanu. Lembani zimenezi mwachidule: _____

_____

_____

Tapimani chomwe mufunukila kuchita. Kodi chigwilizana ndi nchito yopereka ulaliku kwa anthu osowa?

Pamene muyamba ukumana, gawanikani m'magulu ya anthu ANAI pagulu limodzi pampindi zokwanila ngati makumi yatatu mwina mwache mochepekela. Muphephererani wina ndi mzache ndipo mufunsane mafunso ya ungwilo. Pambuyo pache nkhalaninso m'magulu anu ndiku werenga phunzilo ili ndiku ponyapo ndemanga.

Tingawerenge chipangano chatsopano chonse mosamala komabe sitiza peza amulo yomwe ili kulankhula pazomwe azibusa ambili ali kuchita masiku yano . komabe tipezanso azibusa kapena azitsogoleli ambili ali akuchita zina zache zabwino koma sindiyo gawo imene Mulungu anawapasa. Kodi ndichifunisiso chabwanji chimenechi chomwe chili chosayenela chimene atsogoleli ambiri ali kusata? Ena akufuna umanga m'pingo waukulu. Komabe Ambuye Yesu sanatitume kuti ifeyo timange m'pingo waukulu kapena bungwe yamipingo yambiri. Sitiza pezanso lamulo yakuti timange mipingo! Komabe ichi ndi choodi kuti ambiri aise atumiki aMulungu ifunabe uchita zimenezi ? Tapala UTSI TASIYA MOTO. M'pikisano ochokela ku anzathu ndi aziphunzitsi anthu wabweretsa ganizo yakuti uphindulila kapena utukuka mo za utumiki wathu, ndi kumanga ma Chalichi yali ndima membala yambiri mbiri,ndalama zambiri mbiri ndiponso ukhala ochuka. Chilakolako cho pata zimenezi chima bweretsa mabvuto yambiri ndi zina zosa enela ngati mipikisano zomwe Ambuye sanalole. Abale nd Alongo, tiyini tisinthe maganizo yathundiku chita zomwe Mulungu akufuna kuti ise tichite.

NDEMANGA/MAFUNSO: *Kodi mwachita zotani pankhani yakuti mumange m'pingo waukulu?*

Ngati Ambuye Yesu sanatipase nchito m'pingo waukulu kenaka ubyala mipingo, kodi tizachita chiani ise? Ambuye Yesu asanapite kumwamba analankula mo lunjika kuti "timuke ndiku phunzitsa onse amitundu…" Mateo 28:19. Iyi ndiyo nchito ya ikulu imene Mulungu anatipasa. Lingo lathu lalikulu niyakuti ise timuke ukalalika kwa anthu onse am'midzi, m'mizinda zonse ndi muma iko yonse yapansi ndi kuwa phunzitsa ndiponso kuwatuma kuti achulutsi nchito ya Ufumu wa Mulungu. Zimenezi ndizo zitsadzo zimene tipeza mubuku ya Machitidwe. Atumwi ndi Ophunzila onse analalikila uthenga wa Mulungu padziko lonse. Chifukwa cha ulaliki, mipingo zatsopano zinabyalidwa ndipo zinachulukila (welengani Machitidwe 6:1, 7; 9:31; 19:10). Mu za utumiki onse lingo si inali paku byala mipingo komabe kuphunzitsa amitundu. Pamene anaphunzitsa amitundu, kubyala kwa mipingo kuna bwela m'mbuyo. Apa pali kusiyana kwa kukulu. Lingo lathu sikumanga mipingo ya ikulu komabe Uphunzitsa amitundu amene aza chulukila. Tikakhala ndi lingo imeneyi, tizakhala ndi mipingo yabwino ndipo yathanzi imene izachulutsanso mipingo ina!

NDEMANGA/MAFUNSO: *Kodi muzasintha zinthu zotanii mu za utumiki wanu kuti inu muzipereke ku nchito yo chulutsa ophunzilaltiplying (m'malo yo manga mpingo wau-kulu)?*

Ngati tawerenga Mchipangano cha Tsopano tipeza mpingo wa pafupi(simple). Chikhazikizo cha mpingoyu chinalinso chapa fupi ndiponse chapafupi uchulukitsa. Mpingoyo unali otsogoleledwa ndi atsogoleli olimba. (1 Timoteo 3, Tito 1) ndipo unali ndi chikhalidwe chapafupi. Chinali chozipereka mu za utumiki kwa mulungu ndi kwa wina ndi mzache ndiponso upereka umboni ndi kulimbitsana wina ndi mzache welengani 1 Akolinto14, Akolose 3:15-17; 4:2-6). Mstogoleli wina anati mipingo iyi ya nu Chipangano Chatsopano inayanganila pa mitu ya ikulu itatu:

1) Kuzipereka kucho onadi cha Mulungu,
2) Kutumikila ndi kukonda abale mumpingo ndiponso,
3) upeleka umboni kwa anthu apadziko lonse.1

Komabe mpingo wa makono ndi ovuta kwa basi. Zi imikiso ndi zi chitidwe za mpingo kawiri kawiri zitilitsa ifeyo kuti ti kuze a Kristo kuti akhale Ophunzila – chamene chili lingo lomwe mpingo unakhazikitsidwa. Tiyene tisamalile zinthu zomwe ena anga kwanilitse kuti zibalane.

NDEMANGA/MAFUNSO: *Kodi ndi zinthu zotani zomwe tinga chite kuti mpingo yathu ikwanilitsa uchita zinthu zitatu zomwe ta chula?*

Choncho ndi chofunikila kuti tiyike maso yathu pa nchito yo chulutsa Ophunzila m'malo yoti timange mipingo yaikulu. Tikhali ozipereka ku nchito yo panga Ophunzila osati chabe ukhali ndi anthu amene amabwela ku mpingo. Pathawi imodzinso ndi cho unikila kuti tiyike zinthu munjila ya pafupi kuti mipingo yathu ikhale ndi danga yo byala mipingo ina. Lamulo kwa mpingo ili onse ndi uyu: ngati chomwe tichita sichinga chitidwe ndi Ophunzila wina, ndi bwino ku chileka!

NDEMANGA/MAFUNSO: *Kodi ndi zinthu zotani zomwe muku chit mu mpingo wanu zomwe m'kristu wina sangakwanitse kuti achibeleke? Kodi muganiza kuti chinga sokoneze bwanji nchito yo chulutsa Ophunzila?*

Pamene muku lingalila za mfundo zili mu phunzilo ili, ta pimani zi nchito za npingo wanu ndi ku yankha ma funso aya:

ZOCHITA SABATA LINO:

Гsiku 1: ngati mwapenyetsesa zi nchito zonse za utumiki wanu mwezi uyu wa pita kodi mu ngayankhe mfunso iyi mokhulupirika: Kodi mu kutipo bwanji pa funso iyi ngati Abusa kapena Atsogoleli Cha chikulu:

☐ umanga mpingo wa ukulu?

☐ uchulutsa omphunzila?

Kodi nichifukwa ninji mwa mwa pereka yankho iyi?

Гsiku 2: Kodi ndizi nchito zo tani zomwe zikuletsani kuti inu musa thengeko mbali ku nchito yo chulutsa Ophunzila?

Гsiku 3: Ndi ma pologilamu yanji yomwe Ambuye ali kuku tsogolelani kuti musiye kapena kusintha kuti mpingo wanu ukhale wa utumiki wo lalika uthenga kwa anthu osowa?

Гsiku 4: Kodi munga sinthe bwanji chikhalidwe cha mpingo kapena utumuki wanu kut anthu auzindikile mwa pafupi ndiponso kuti azitsogoleli am'tsogolo agwilitse chitsanzo chanu?

Neil Cole, Organic Church, Chapter 8.

MPHUNZILO 4 - UTUKULA ZA UMOYO

"DZADZANI UMOYO WANU NDI MAU AMULUNGU"

Pamene muyamba ukumana, gawanikani m'magulu ya anthu ANAI pagulu limodzi pampindi zokwanila ngati makumi yatatu mwina mwache mochepekela. Muphephererani wina ndi mzache ndipo mufunsane mafunso ya ungwilo. Pambuyo pache nkhalaninso m'magulu anu ndiku werenga phunzilo ili ndiku ponyapo ndemanga.

Maziko yolimba pa umoyo wa chi Kristo ndi umoyo wa Utumiki ndi kudziwa ndi ku gonjela mau aMulungu. Mulungu anati pasa Mau Ache kuti "munthu wa Mulungu ankhale woyenera, wokonzeka kuchita nchito iri yonse yabwino." (2 Timoteo3:16-17,). Kodi tinga khale bwanji wokonzeka ku pitila ku mau a Mulungu? Baibulo iti sonyeza njila zisanu ndi imodzi momwe tinga dzadzile umoyo wathu ndi maganizo yathu ndi mau a Mulungu.

<u>Choyamba</u>, tiyenera **kumva** mau aMulungu. Mzinda wonse wa Isilayeli inali kumva mau a Mulungu pamene yanali kuwerengedwa(Yoshua 8:34-35). Paulo ana uza told Timoteo kuti azi werenga malemba kwa onse (1 Timoteo 4:13). Tonsefe ifunika ku werenga mau a Mulungu ndi kumvanso ena ali kuwerenga. Tengani nthawi inu mabanja yanu kuwerengelani mau kwa wina ndi mzache kapenanso kumva mau pa makina ya Wailesi. Tifunika kumva mau a Mulungu!

NDEMANGA/MAFUNSO: *Ndi njila zotani zimene muna peza kuti zilibwino kwa inu kuti mumvetsetsetse malemba?*

<u>Chachiwili</u>, tiyenela **kuwerenga** Baibulo. Mafumu yonse yakale ya Isilayeli yana udzidwa kuti yalembe buku ya malemba ya Mulungu pa iwo okha, kuti 'awerenge pa masiku ya moyo wao onse," (Deuteronomo 17:18-19). Mpingo naonse una lamulilidwa kuti uwerenge makalata ya Chipangano Chatsopano (Akolose 4:16). Tifunika kuwerenga malemba ya Baibulo yonse kawili kawili. Tikuku limbitsani kuti inuzi werenga malemba ya kwanila ngati ma chapitala ma Khumi Yawiri ndi Yasanu kufikila ku Makhumi Yatatu sabata iliyonse.

NDEMANGA/MAFUNSO: *ndi phindu yotani yomwe muzapeza gati inu ndi abale ena am'mupingo mukuwerenga ma chapitala ma khumi ya wiri ndi yasanu kapena Makhumi yatatu sabata iliyonse (Ma chapitala ya tatu kapena yasanu pa siku iliyonse?*

<u>Chachitatu</u>, tifunika **phunzilani** Baibulo. Ezara "anadzipereka ku kawerengedwe ka mau to ndi kutsata ma lamulo ya Mulungu," (Ezara 7:10). Mwamuna kapena Mzimai wa Mulungu afunikila kusata, kumasulila ndi ku mvetsetsa

nalemba kuti tidziwe ku khala m'chilungamo (2 Timoteo 3:16-17). Tifunika upeza nthawi siku ndi tsiku kuwerenga mau a Mulungu nthawi ndi nthawi.

NDEMANGA/MAFUNSO: *kodi kuwerenga ndi ku santhula mau ku siyana poti?*

Chachinai, tifunika **ukumbukila** malemba mwa chi zowelezi. m'nyamata asunga nau a Mulungu m'mtima mwache kuti asa chimwile Mulungu, (Masalimo 119:11). Yesu ana gonjetsa Satana po lankhula mau yamene anasunga mu mtima mwache. Mateyu 4:4, 7, 10). Tilimbisa inunso kuti mulingalile ndime imodzi yokha pa sabata imodzi. Njila imodzi yomwe ya simikidzidwa ndi anthu ena, ndiku werenga ndime mo kuwa kasanu ndi kawiri pa siku.

NDEMANGA/MAFUNSO: *Mu kumbuke mwa nthawi zonse Yoswa 1:8 sabata lino. Mu werenge ndime iyi mu kuwa kasanu ndi kawiri manje manje!*

Chachisanu, tifunikila **kulingalila** pamalemba . ambuye Mulungu ana uza Yoswa kuti alingalile malemba usana ndi usiku.(Yoswa 1:8). masalimo1 ilankhula kuti umoyo wa phindu ndi umoyo wo chulukila umabwera kamba ko linglila malemba. Ulingalila chi thanthauza upereka maganizo yathu mozama kuti tidziwe tanthauzo ya nalemba ndi njila yomwe tingasinthile umoyo wathu kulingana ndi mau yomwe ikuwerenga. Kulingalila ndi ku kumbukila malemba ziyenela kuyenda pamodzi

Chisanu ndi chimodzi, tifunikila **ku sewenzetsa** kapena **kunverera** Baibulo. Mulungu anatipasa mau yache kuti yati sinthe iseyo. Njila zonse izi zimene tacchulu ingo lache niyakuti zitithandizile ku khali mu choonadi cha malemba (Werenganinso ndime izi kuti muone ichi). Ngati ise siti sewenzetsa malemba Yakobo akuti ndise achinyengo (Yakobo1:22-25).



NDEMANGA/MAFUNSO: *Ndi malemba yotani yomwe Mulungu ali kuyika pa mtima wanu kuti inu muwasewenzetse panthawi?*

Chitsanzo cha bwino chimene chingathe kuti thandiza kuti tikumbuku izi njila zisanu ndi modzi ndi Dzanja lanu. Chala chili chonse chi milila njila zisanu zoyamba ya kasiwenzetsedwe ka Baibulo, ndipo dzanja? - I imililа njila ya chisanu ndi chi modzi- kuti tisewenzetse ndi ku gonjela mau ya Baibulo. Tika gwilitsa chito izi njila tiza mphindulila kwa mbili!

ZOCHITA SABATA LINO:

Tsiku 1: Sewenzetsani dzanja lanu tsiku ndi tsiku kuti mukumbuke kasewenzetsedwe ka Baibulo. Sewenzetsani izi njila zisanu ndi imodzi. Penyetsetsani mu bokosi ili tsiku ndi tsiku.

☐ *Sondo* ☐ *Loyamba* ☐ *Chibili* ☐ *Chitatu* ☐ *Chinai* ☐ *Chisanu* ☐ *Chibelu*

Tsiku 2: Panjila zonse izi zisanu ndi imodzi, ndi iti njila yomwe muzafunikila kuti musamale bwino?

Kodi mu zazichita bwanji zimenezi?

Tsiku 3: Zindikilani ndikudziwa njila imodzi yapadela imene mungagwilitsile nchito pakati pa izi njila zisanu ndi imodzi powerenga Buku lopatulika.

Njila #1:

Njila #2:

Njila #3:

Njila #4:

Njila #5:

Njila #6:

Tsiku 4: Lingalilani Yoswa 1:8.

Pamene muyamba ukumana, gawanikani m'magulu ya anthu ANAI pagulu limodzi pampindi zokwanila ngati makumi yatatu mwina mwache mochepekela. Muphephererani wina ndi mzache ndipo mufunsane mafunso ya ungwilo. Pambuyo pache nkhalaninso m'magulu anu ndiku werenga phunzilo ili ndiku ponyapo ndemanga.

Muphunzilo ya chiwiri , tina longosola kuti utsogoleli ndiku takasa anthu kuti achite zomwe zaikidwa. Muphunzilo ili, tiza ika maganizo yathu pa zinthu zimene zimapanga mtsogoleli.

Kodi Mtsogoleli Ndani?

Mtsogoleli ndi munthu wamene adziwa zo onadi zitatu:

[1] Adziwa komwe akupita,
[2] Adziwa njila ndiponso,
[3] Adziwa motakasila anthu kuti amuke nai pamodzi.

Choyamba, mtsogoleli adziwa komwe akupita ndiponso ali ndi lingo pazomwe akuchita. Mtsogoleli akhala ndi chithunzi chazinthu zomwe afuna kuti zichitike. Ndiponso samango dziwa komwe akupita komanso njila zomwe azachita kuti akwanilitse zomwe alingalila. Motsiliza, mtsogoleli adziwa motakasila anthu kuti amutsatile ndiku chita zomwe alingalila. Munthu yemwe sadziwa utakasa anthu ena kuti amuthandize kuti akwanilise zomwe afuna ukwanilisa, munthuyo simutsogoleli ai. zi zinthu zitatu ndizofunikila mu umoyo wa mtsogoleli.

NDEMANGA/MAFUNSO: *Kodi ngati modzi wa izi palibe zinga ononge bwanji utsogoleli?*

Mfundo zitatu zofunikila mu umoyo wa Mtsogoleli:

[1] = MASO MPHENYA: kudziwa njila

[2] = NDONDOMEKO: Udziwa njila, kapena mochitila zinthu

[3] = MCHANGU: kudziwa motakasila ena kuti agwile nchito ya Mulungu

NDEMANGA/MAFUNSO: *kodi tinga chite bwanji kuti tikwanilitse mfundo zitatuzi zotithandizila ise kuti tikhale azitsogoleli abwino?*

ZOCHITA SABATA LINO:

